Kodi Munthu Akafa Amapita Kuti? (Gawo 1)

Nkhaniyi yachokera m'mutu 6 wa buku lakuti, *Kodi Baibulo Limaphunzitsa Chiyani Kwenikweni?* lomwe likupezeka pa jw.org/ny.

CHOLINGA: Ganizirani mozama zimene mumakhulupirira ndiponso zifukwa zake, fufuzani zimene Baibulo limaphunzitsa, kenako ganizirani mmene mungafotokozere ena zimene mumakhulupirirazo.

KODI CHIMACHITIKA N'CHIYANI MUNTHU AKAMWALIRA?

1 GANIZIRANI MOZAMA ZIMENE MUMAKHULUPIRIRA

Kodi mukuganiza kuti anthu ena angayankhe bwanji?

Kodi **inuyo** mumakhulupirira zotani?

Nanga n'chifukwa chiyani mumakhulupirira zimenezo?

www.jw.org © 2015 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania

2 FUFUZANI ZIMENE BAIBULO LIMAPHUNZITSA

Munthu akafa, sakhalanso ndi moyo kulikonse.

(Werengani mutu 6 m'buku lakuti *Baibulo Limaphunzitsa Chiyani*, ndime 1 mpaka 6.)

Werengani Mlaliki 9:5, 10.

Kodi mavesi amene mwawerengawa akusonyeza bwanji kuti munthu akafa palibe chimene chimapitiriza kukhalabe ndi moyo?

Kodi zimene zimachitika munthu akamwalira, mungaziyerekezere ndi chiyani pofuna kusonyeza kuti **samakakhalanso** ndi moyo kwina kulikonse?



Moto wakandulo ukazimitsidwa *supitanso* kulikonse. Umangothera pompo. Mofananamo, munthu akamwalira sakhalanso ndi moyo kwina kulikonse

www.jw.org © 2015 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania

Imfa ili ngati tulo tofa nato.

(Werengani mutu 6 m'buku lakuti *Baibulo Limaphunzitsa Chiyani*, ndime 7 ndi 8.)

Werengani Yohane 11:1-14.

Kodi inuyo mukuganiza kuti n'chifukwa chiyani Yesu anayerekezera imfa ndi kupumula?

Werengani Machitidwe 7:60 ndi 1 Akorinto 15:6.

Kodi mavesiwa akusonyezanso bwanji kuti munthu akafa amakhala ngati wangogona tulo?

Kodi n'chifukwa chiyani inuyo mumasangalala kuti mumadziwa zimene zimachitika munthu akamwalira?

www.jw.org © 2015 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania

3 FOTOKOZANI ZIMENE MUMAKHULUPIRIRA

WINA AKANENA KUTI . . .

Munthu akamwalira amakakhalanso ndi moyo kwina kwake.

MUNGAYANKHE KUTI . . .

Zipembedzo zambiri zimaphunzitsadi zimenezo. Koma ine ndimakhulupirira zosiyana ndi zimenezo chifukwa . . .

_____

_____

Kodi mungawerenge lemba liti kuti mumuthandize?

_____

Kodi mungafotokoze bwanji vesilo pomuthandiza malinga ndi zimene amakhulupirirazo?

_____

WINA AKANENA KUTI . . .

Mulungu amalanga anthu oipa powaotcha ndi moto.

MUNGAYANKHE KUTI . . .

N'zoona kuti Mulungu adzalanga anthu oipa. Koma ine sindimakhulupirira kuti amawaotcha ndi moto chifukwa . . .

_____

_____

Kodi mungawerenge lemba liti kuti mumuthandize?

_____

Kodi mungafotokoze bwanji vesilo pomuthandiza malinga ndi zimene amakhulupirirazo?

_____

www.jw.org © 2015 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania